**SOUTH EAST EDUCATION DIVISION**

**2024 MALAWI SCHOOL CERTIFICATE OF EDUCATION**

**CHICHEWA**

**PAPER III-MARKING KEY**

**Gawo A (Malikisi 30)**
**Nkhani za Mchezo ndi zolembedwa**
**NDAKATULO**

a. kodi akuyankhula mu ndakatuloyi ndani?
   - Amayi ake Naduwe. / kholo la chikazi **(1 Malikisi)**

b. Tchulani zinthu **ziwiri** zomwe woyankhulidwa akukana kuchita n'ndakatuloyi?
   - Kupita kukatunga madzi ku chitsime **(1 Malikisi)**
   - Kupita kolima **(1 Malikisi)**

c. Tsimimkizani popereka mfundo **imodzi** kuti yemwe akuyankhulidwa m'ndakatuluyi ndi wamwano.
   - Akumalalatira ngakhale mayi ake omubereka **(2 Malikisi)**

d. Perekani zipangizo **zitatu** zimene mlembi wagwiritsa ntchito mu ndakatuloyi
   - Mvekero
   - Zining'a
   - Mikuluwiko
   - Kusinira mawu
   - Zifanifani

   **(Zitatu mwa izo ndipo 1 malikisi yankho lililonse = 3)**

- Kamvekedwe kodandauala: woyankula: woyankhulayu sakusangalala ndi khalidwe losamvera la mwana wake **(2Malikisi )**

c. Perekani matanthauzo a mawu awa:

i. Kusanakupindulire
   - Kusanakupindulire moyipsa **(Malikisi 1)**

ii. Palasupalasu
   - Kukhala mosakhazikika/ kusakhazikika malo amodzi **(Malikisi 1)**

iii. Waphuka
   - Walemera **(Malikisi 1)**

iv Perekani phunziro lopezeka m'ndakatuloyi?
   - Ndibwino kulemekeza makolo/ osamachitira mwano anakubala **(Malikisi 1)**

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

1. **NKHANI YAYIFUPI**

a Kodi nkhaniyi ikuchitikira kuti?

- M'mudzi mwa Dokerwa **(Malikisi 1)**

b. Perekani mphendero ya nkhaniyi?

- Yakambazawina **(Malikisi 1)**

c. Tchulani mavuto atatu omwe Gogo Goloso adakumana nawo paukalamba wao

- Kunamiziridwa zoti amanga mvula **(Malikisi 1)**
- Kunenedwa kuti ndi mfiti yaikulu **(Malikisi 1)**
- Kusasuka kwa denga la nyumba yake **(Malikisi 1)**

d. Tsimikizani kuti Babache anali wopanda ulemu

- Adawatchula gogo goloso kuti ndi mfiti
- Adafunsa gogo Goloso chifukwa chomwe sasambira
- Sadakhale nkomwe pansi pomwe amayankhula ndi gogo Goloso

**(awiri mwa mayankhowa, 1 malikisi yankho lililonse=2 malikisi)**

e. Fotokozani mfondo **ziwiri** zopezeka m'nkhaniyi

- Nkhaza: anthu a m'mudzi mwa mfumu Dokerwa anawanamizira gogo Goloso kuti adamanga mvula **(2 Malikisi)**
- Zikhulupiriro: anthu a mudzi wa mfumu Dokerwa amakhukulupirira azimu ndipo adakathira nsembe kuti mvula ibwere ./Kukhulupirira a sing'anga komanso ufiti **(2 Malikisi)**
- Kumutengera kubwalo la mfumu mokakamiza akudwala. **(2 Malikisi)**

**(awiri mwa mayankhowa, 2 malikisi yankho lililonse=4 malikisi)**

f. Perekani matanthauzo a nsinjiro za chiyankhulo izi:

Mtunda wopanda madzi

- Zinthu zotsathandiza **( 1 Malikisi)**

Akumva mthupi

- Akudwala **( 1 malikisi)**

Kumbiya zadooka

- Kumanda **( 1Malikisi)**

Adagwidwa ndi mutu wa zizwa

- Anadabwa **( 1Malikisi)**

**GAWO B (MALIKISI 40)**

**Langizo:** Yankhani mfundo **zinai** zosonyeza kuti Nthondo adakumana ndi mavuto osiyanasiyana m'bukhu la Nthondo **(20 Malikisi)**

- Kutsekeredwa mu mu gadi

Mafunso akupitirira/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

**i.** Nthondo adakakhala m'gadi masabata atatu chifukwa chokuba maungu kwa mzungu

**ii.** Nthondo adakakhala m'gadi miyezi isanu ndi umodzi kaamba komenya mnzake mpaka kumukomola

- Kusalidwa

i. Nthondo amasalidwa ndi atsibweni ake kaamba ka khalidwe lake loipa

**ii.** Mai ake a Nthondo adamusala nthondo chifukwa cha khalidwe lake loipa

**iii.** Anzake a Nthondo anamuthawa pa ulendo wa ku Harare kaamba ka khalidwe lake lakuba

- Kulota maloto oipa

i. Nthondo analota atate ake atapha nsomba ndipo atawapempha anamumana nanena naye kuti sindiwe mwana wanga

ii. Nthondo analota mnzake yemwe adafa atapita naye kukaba misinde

iii. Nthondo adalota atapita ku uzimba ndipo mikango iwiri idayamba kumupitikitsa ndi kumudya

- Kumenyedwa

i. Nthondo adamenyedwa ndi anzake paulendo kaamba ka ulesi ndi mwano

ii. Nthondo adamenyedwa atagwidwa akuba nkhuni ku Kapata ndi mwini nkhuni

**Kapena**

b. Tsimikizani popereka mfundo **zinai** kuti amapangankhani ena anali olimba mtima **(20 Malikisi)**

- Bambo ake a Nthondo ndi anzawo

i. Adagwidwa ndi asilikali kuti akonze ulalo omwe a Nyalapa adakokolokapo ndi madzi

ii. Adazimangira okha msasa kuti agonemo nthawi yomwe udzu udali ouma

- Nthondo ndi anzake

i. Adayenda ulendo wa ku Harare ndipo anaoloka mitsinje yoopsya

ii. Amanyamula katundu mitunda yaitali

- Nthondo

i. Anatembenuka mtima ndikukhala mkhristu

ii. Anathetsa mzinda m'mudzi wa a Chembe

iii. Anavomereza sukulu m'mudzi wa a Chembe



Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

- Munthu yemwe adamubela katundu
  - i. Adathawisa katundu wa Nthondo osaoneka
  - ii. Adamubera Nthondo akuona ndipo Nthondo adapereka yekha katunduyo

**CHAMDOTHE NDI ZISUDZO ZINA**

**(W. Nkhoma, S. Likongwe)**

**MCHIRA WA BULUZI**

1. a. Tsimikizani popereka mfundo zinayi kuti Ndileya ndi Nadzonzi adataya mfungulo ya ukwati wachisangalalo **(Malikisi 20)**

- Amachitirana nkhaza
  - i. Ndileya amamumenya Nadzonzi popanda chifukwa chokwanira
  - ii. Nadzonzi anamuthirira mankhwala a mkala wa buluzi mu mowa wa mwamuna wake kuti azimukonda
  - iii. Ndileya anagulira Nazunga nyama ya ng'ombe pomwe mkazi wake ndi ana anadyera masamba a nkhwani
- Awiriwa samasamalana
  - i. Nadzonzi samachapa zovala za Ndileya ngakhale iye amamupatsa sopo
  - ii. Ndileya anamugulira Nazunga nyama malo moti agulire Nadzonzi mkazi wake
- Samapatsana ulemu
  - i. Ndileya amamumenya Nadzonzi
  - ii. Ndileya ndi Nadzonzi samayankhulana bwino, amanyozana.
- Ndileya anali pa ubwenzi wamseri ndi Nazunga
  - i. Ndileya anatha mwezi akugona ku nyumba kwa Nazunga
  - ii. Ndileya amafuna kuthesa banja kuti akwatire Nazunga

**ZIKANI**

b. Fotokozani mfundo **zinayi** zosonyeza nkhaza atengambali osiyanasiyana mchisudzochi **(20 Malikisi)**

- Mgezenge
  - i. Mgezenge adamumenya Nagama popeza iye sankalowa mnyumba pomwe Nagama ankadwala.
  - ii. Mgezenge ankamugwiritsa ntchito ankamugwiritsa Funsano m'golosale ndipo amamulipira zovala zakale
  - iii. Mgezenge adamukwenya pakhosi Funsani atamupeza ndi cholembera ndipo malipiro ake sadamupatse



Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

- Abiti ndi Gama
  i. Abiti ndi Gama adamuuza Zikani kuti asiye sukulu kuti asangalase a Mgezenge
  ii. Abiti ndi Gama adamupereka Zikani kwa a Mgezenge ngati shazi
- Kamwendo
  i. Anasiyitsa ana awo sukulu pena kuwajombetsa ku sukulu
  ii. Amagwiritsa ana awo ntchito zobyolera misinkhu yawo
- Makolo ake a Chisomo
  i. Adamupereka kwa a Mwenechanya ali ndi zaka zisanu ndi ziwiri
  ii. Anamusiyitsa sukulu kuti akhale mkazi wachinayi wa a Mwenechanya
- Akuluakulu a m'maesiteti
  i. Amagwiritsa ana ntchito zolemetsa zobyolera misinkhu yawo
  ii. Amasiyitsa ana sukulu

**(mfundo zazikulu zinayi zokha mwa zimenezi)**

- ✓ Chiyambi- **(2 Malikisi)**
- ✓ Thunthu- **(1 Malikisi)**
  i. Mfundo zazikulu **(2 Malikisi)** ndipo zikhalepo zinayi
  ii. Mfundo zotsindika mfundo zazikulu zikhalepo ziwiri pa mfundo imodzi yayikulu **(1 Malikisi)** iliyonse = **2 Malikisi**
- ✓ Mathero- **(2 Malikisi)**



Downloaded for **FREE** from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com